# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA CHIRADZULU M'DZINJA LA 2024-2025

## Dzinja la 2024/25 Mwachidule


Nyengo ya mvula ya 2024-2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira koposa mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.
Boma la Chiradzulu likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera mlingo wokhazikika.

## October 2024





Nyengo yopanda mvula ikuyembekezereka m'madera ambiri. Ndipo mvula ya Chizimalupysa yofikira mulingo wa 70 mm ikuyembekezereka m`madera ena.
Mvulayi ndiyokhazikika kapena kupyolera ndipo ikhoza kuposera mwezi womweu chaka chatha.

## November 2024





Mvula ya mlingo wokhazikika komanso kuchepera ikuyembezereka. Madera ena akhoza kudzalandira mlingo wa pakati pa 30 ndi 50 mm.
Madera ena a TA Likoswe ndi TA Nchema akhoza kuzalandira mvula yochepera mlingo okhazikika. Nyengo yadzinja ikuyembekezeka kuyamba sabata lomaliza la mweziwu.

## December 2024





M'mwezi wa December, mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera ikuyembekezereka m'madera ambiri yomwe ndi ya mlingo wapakati pa 160 ndi 270mm. Mvulayi ndiyochulukirapo kuposera dzinja lapita. Komabe, ku m`mawa kwa bomali kukhoza kuzagwa mvula ya mlingo wocheperako

## January 2025




January akuyembekezereka kudzalandira mvula yochuruka kuposa miyezi yonse ya dzinjali ngakhalenso dzinja la chaka chatha. Kwa TA Likoswe ikhoza kupyola 300 mm koma kummwera kwa TA Nchema ikhoza kuzacheperapo ndi mlingo wa 150 mm.
Ng'amba ya sabata limodzi ikuyembekezereka m'mweziwu.

## February 2025





**Mvula yochepa yapakati pa 100 ndi 150mm** ikuyembekezekereka m'madera ambiri.

Ndipo madera a kwa TA Nkalo, Kadewere ndi pa Chiradzulu boma akhoza kudzalandira mvula **yofikira mulingo wa 100mm**.


**Ng'amba ya sabata limodzi l**ikuyembekezereka m'mweziwu.

## March 2025




Mvula ya mulingo wokhazikika komanso kupyora ikuyembekezereka m`bomali. Koma mvula yambiri yofikira mulingo wa 200mm ikuyembekezekereka m'madera a a kumpoto monga TA Chitera komanso kum`mwera kwa TA Nkalo.M`madera ambiri a pakati ndi kum`mawa ayembekeze mlingo wapafupifupi 100 mm

## April 2025





Mvula ya mulingo wokhazikika kapena kuposera koma yosapyola 90mm ikuyembekezereka m'madera ambiri.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kutha pofikira mkatikati mwa mwezi wa April.

- Nyengo ya dzinja m'boma la Chiradzulu ikuyembekezereka kuyamba pakati pa sabata yotsiriza ya November ndi sabata yoyamba ya December 2024. Nyengo ya dzinjayi ikuyembekezereka kutha pakati pa sabata yachiwiri ndi sabata yachinayi ya mwezi wa April 2025. Ng'amba ya sabata limodzi mu mwezi wa February ikuyembekezeredwa. Nyengo ya dzinjayi ikuyembekezeleka kukhala ya masiku a pakati pa 120 ndi 140.

**MOMBEZI**

| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
|---|---|---|---|
| OCT | 2.7 | 16.6 | 12.9 |
| NOV | 38.8 | 64.4 | 40.7 |
| DEC | 123.8 | 182.4 | 150.4 |
| JAN | 175.2 | 229.6 | 206.7 |
| FEB | 128.3 | 202.5 | 221.9 |
| MAR | 74.8 | 138.0 | 200.3 |
| APR | 14.1 | 37.0 | 38.7 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

The Development Fund